EXAMINATION NO.: ____________

# THE MALAWI NATIONAL EXAMINATIONS BOARD

2026 MALAWI SCHOOL CERTIFICATE OF EDUCATION EXAMINATION

# CHICHEWA

Subject Number: **M032/II**

Tuesday, 7 July

Time Allowed: 2 hours
1:00 - 3:00 pm

## PAPER II

(Malikisi 90)

**Malangizo:**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi atatu.**

2. Pepalali lili ndi magawo anayi: **A, B, C** ndi **D.** Yankhani mafunso onse m'magawo onsewa.

3. Lembani **nambala yanu yamayeso** pamwamba pa tsamba **lililonse la pepalali.**

4. Muchitebulo chili pambalichi, onetsani funso lililonse lomwe mwayankha kuyambira **funso 1 mpaka 7** pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.

5. Perekani pepalali kwa oyangánira mayeso nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani funso ngati mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6 | | | |
| 7 | | | |
| | | | |
| | **Total** | | |


©2026 MANEB
Turn over

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## Gawo A (Malikisi 40)

## Malamulo a Chiyankhulo

**Langizo:** Yankhani mafunso onse m'gawoli pa mizere yomwe yaperekedwa pa funso lililonse.

1. a. Tchulani mitundu ya aperekezi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

    (i) Mwanayu adabadwa pa 7 Julaye chaka chatha.

    ______

    (ii) Iwo adali m'kati mwa nyumbayo pamene mvula inkagwa.

    ______

    **(Malikisi 2)**

   b. Sinthani mimvekero yomwe yatsekedwa mzere kunsi kwawo kuti ikhale aneni m'ziganizo zotsatirazi.

    (i) Buluzi adangoti lowu ku una.

    ______

    (ii) Zinthu zinali balala pabwalo.

    ______

    (iii) Mwanayo anangoti terereku ali pansi.

    ______

    (iv) Njoka inangoti phofo kugwa kuchokera mu mtengo.

    ______

    **(Malikisi 4)**

   c. Pangani ziganizo zomveka bwino posonyeza kachitidwe ka aneni kotsatiraka ndipo mutseke mzere kunsi kwa aneniwo.

    (i) kachitidwe kawochita

    ______

    (ii) kachitidwe kawochitidwa

    ______

    **(Malikisi 4)**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Mafunso akupitirira/…

2. a. Pezani aneni m'ziganizo zotsatirazi ndipo mutchule nthawi ya aneniwo.

(i) Anyani adya chimanga chonse.

Mneni: ____________________

Nthawi ya mneni: ____________________

(ii) Iye adzakhala akutunga madzi tsiku lonse.

Mneni: ____________________

Nthawi ya mneni: ____________________

(iii) Mnyamatayu ankasewera mpira kwambiri.

Mneni : ____________________

Nthawi ya mneni : ____________________

**(Malikisi 6)**

b. Lembani ntchito zomwe 'ti' yemwe watsekedwa mzere kunsi kwake akugwira m'ziganizo zotsatirazi.

(i) Agogo aku<u>ti</u> mphaka wadya ndiwo zonse.

____________________

(ii) <u>Ti</u>mbale tokongola tija tasowa.

____________________

(iii) Ife <u>ti</u>makonda kuvina magule a chikhalidwe chathu.

____________________

(iv) Kodi iwe ukufuna tinkhuku ti<u>ti</u> ?

____________________

**(Malikisi 4)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

3. a. Pangani ziganizo zomveka bwino ndi "lima" pofuna kusonyeza mitundu ya mawu yotsatirayi ndipo mutseke mzere kunsi kwa mawuwo.

(i) mneni

______________________________

(ii) mfotokozi

______________________________

(iii) dzina

______________________________

**(Malikisi 6)**

b. Fotokozani momwe mayina otsatirawa adapangidwira.

(i) umwini

______________________________

______________________________

(ii) myang'anadzuwa

______________________________

______________________________

**(Malikisi 4)**

4. a. Sinthani ziganizo zotsatirazi kuchoka mu zoyankhula wina kupita mu zoyankhula mwini.

(i) Aphunzitsi adatiuza kuti tidzabwere tsiku lotsatiralo.

______________________________

______________________________

(ii) Asilikali adatifunsa chomwe tinkachita pamenepo.

______________________________

______________________________

(iii) Mwayi adafuula kuti tiyike zinthuzo pansi.

______________________________

______________________________

**(Malikisi 6)**

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

4. **(Mafunso akupitirira)**

b. Tsekani mzere kunsi kwa nthambi yosaima payokha m'ziganizo zotsatirazi ndipo mutchule mtundu wake.

(i) Ankalimbikira kuwerenga kotero adakhoza bwino mayeso.

Mtundu wake: ______________________________________________

(ii) Zoti adapambana mayeso ndizoona.

Mtundu wake: ______________________________________________

**(Malikisi 4)**

**Gawo B** (Malikisi 20)

**Kumvetsa Nkhani ndi Kusanthula Chiyankhulo**

5. **Werengani nkhani ili m'munsimu mosamala ndipo muyankhe mafunso otsatirawo pamizere ili pansi pa funso lililonse.**

**MTIMA WAMNZAKO NDI TSIDYA LINA**

Ndinkalephera kumvetsa zomwe Madalo adandichitira ine. Malingaliro ofuna kumwa chiphe adali pafupi nditangotsiriza kuwerenga kalata imene Madalo adalemba n'kuiponya papilo wa pakama kuchipinda kwathu. Mafunso ankhaninkhani ankayandama m'mutu mwanga koma ankachoka ngati nkhungu opanda mayankho. Zina mwa zomwe Madalo adandilembera m'kalata yake yamchokeroyo zidali izi:

*"Dandaula, ndafuna kukuthokoza kwambiri ponditola ine panthawi yomwe moyo wanga udalibenso chiyembekezo. Udandionetsa chikondi chenicheni. Dziwa kuti ndiwe munthu wabwino kwambiri ndipo sindidzakuiwala. Ndikukulimbikitsa kuti uyesetse kudzipezera mkazi wabwino, wokuyenera iwe. Ine ndalephera kukhala mkazi wabwino. Ngakhale ndinkayesera kuti ndibwezere chikondi chimene unkandipatsa, ndinkakanika chifukwa chikondi changa chidali chonama komanso chogawanika kuyambira pachiyambi.*

*"Ndakhala ndikukunamiza kuti Mayeso adatchona ku Ulaya. Mayeso ali m'dziko*



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

5. **(Mafunso akupitirira)**

*momwe muno. Ndidakhala ndikumenya nkhondo yakuti achokeretu m'maganizo mwanga koma ndagonja moti kwa nthawi yayitali takhala tikuzemberana kufikira kuti sitingathenso kupitiriza mchitidwewu. Mavuto si mwana wako ayi koma wa Mayeso."*

Ndidawerenga kalata ija mobwerezabwereza ndi chiyembekezo chakuti uthenga udali m'kalatayo usintha. "Wachitiranji izi, Madalo? N'zoona Madalo ankanamizira kundikonda? Kodi kapena ndidadya mfulumira kum'kwatira?"

Padali patangotha zaka ziwiri chikwatiriraneni mmene Madalo adanditulukira m'nyumba. Ndikukumbukira ukwati wathu udali wapamwamba kwambiri kotero kuti abale ndi anzathu ena ankatithiramo kuti adali asadaone ukwati ngati wathuwo m'dera lathu lonse. Udalidi manthu wa maukwati ndipo tidafapo kuti ukwati wathu utheke. Tonse tidatenga ngongole kuntchito, ngongole zimene tidzakhala tikulipirabe zaka zitatu zikubwerazi.

Mmene tinkamangitsa ukwati wathu, Madalo adali woyembekezera kwa miyezi itatu. Mavuto atabadwa anzathu ankatisinjirira kuti tidali adani a kulera. Izi sizidatidetse nkhawa chifukwa panthawiyo chikondi chathu chidali chitafika pachiindeinde. Padalibe chomwe sitinkachitira limodzi moti tidavala dzina loti "ngumbi zothothoka mapiko" chifukwa nthawi zonse tidali londolondo kulikonse tinkapita: kaya kuntchito, kuchipatala, kumsika, kutchalitchi ngakhale kumasewero osiyanasiyana.

Chiyambi cha ubwenzi wanga ndi Madalo chidali chochititsa chidwi kwambiri. Tidakumana kusukulu ya ukachenjede ku Zowa. Ndidali m'chaka chachiwiri pamene Madalo adali m'chaka chachitatu. Tsiku lina nditapita kukawerenga madzulo ku nyumba yowerengera mabuku ndidam'peza iye akulira. Zidandikhudza kwambiri kuona chiphadzuwa chikulira choncho. Ndidafika pafupi n'kuyamba kumutonthoza. Ndidayesera kumfunsa chidatsitsa dzaye kuti njovu ithyoke mnyanga choncho koma patsikulo sadandiululire chimene chidamuchitikira. Adandipempha kuti ndimuperekeze kumene amagona. Ndidavomera mopanda kuwinya kulikonse.

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Mafunso akupitirira/…

5. **(Mafunso akupitirira)**

M'mawa wa tsikulo ndidapita kuchipinda cha Madalo kuti ndikaone momwe adadzukira. Adandilandira ndipo tidacheza mopanda nkhawa iliyonse yadzulo lakelo. Pang'onopang'ono tidayamba kumasukirana ndipo kucheza kwathu kudagwira msewu. Ngati Madalo sabwera kuchipinda changa, ndiye kuti idali nthawi yanga yoti ndikatandale kuchipinda kwake. Kucheza kwathu kudasefukira kumaphunziro. Ngakhale tidasiyana chaka chimodzi, kudapezeka kuti tinkatenga maphunziro ofanana. Tonse tinkafuna kudzakhala akachenjede a zachuma. Ndidazindikiranso kuti Madalo sadangokongola kokha komanso adali wanzeru kwambiri. Tikamakambirana za maphunziro, ankandidolola ndi mmene ankatsitsira mfundo zake. Izi zinkandimvetsa kukoma chifukwa nanenso anthu ankanditayira kamtengo kuti ndidali mphongo pa phunziro la zachuma.

Chochititsa chidwi china chidali chakuti tonse tidali kuchokera ku mabanja okhupuka ndithu. Makolo anga adali ndi kampani yopanga nsapato yotchedwa Khwaila Shoes pamene bambo ndi mayi a Madalo adali oweruza milandu ku bwalo lalikulu m'dziko muno. Moyo wathu kusukulu udali wofewa zedi.

Zoyamba ubwenzi ndi Maliya ndidazitayira kunkhongo. Ndinkaopa kudana ndi njoleyi choncho ndidasankha kukhutitsidwa ndi kukhala mnzake basi. Madalo adayamba kundionetsa moyo opyola chibwanawe. Tsiku lina mopanda choyambitsa adandiululira chimene chidachitika kuti ndimupeze akulira m'nyumba yowerengera mabuku muja.

Madalo adati adali paubwenzi ndi Mayeso, mnyamata amene adali pa sukulu ya ukachenjede yomweyo. Mayeso adali chaka chachinayi pamene Madalo adali chaka chachiwiri. Mayeso ankatenga phunziro la zamalamulo. Mmene ankatsiriza maphunziro ake, ubwenzi wawo udali utafika pampondachimera. Mayeso atayamba ntchito, ubwenzi wawo udapititirabe ndipo awiriwa ankayenderana.

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

5. **(Mafunso akupitirira)**

Patangotha chaka chimodzi chimalizire maphunziro ake, Mayeso adapeza mwayi wokapitiriza maphunziro ake ku Ulaya ndipo adasonyeza kukayika zoti adzabwereranso kumudzi. Adamulimbitsa mtima Madalo kuti adzachita chotheka kumuitanitsa kuti naye adzapite ku Ulayako. Izi zidampatsa Madalo mangolomera wolimbikira maphunziro ake.

Tsiku limene ndidampeza akulira lija, padali patangodutsa miyezi isanu ndi itatu Mayeso atapita ku Ulaya. Akuti patsikulo, Mayeso adamtumizira uthenga wa palamya ya m'manja womuuza Madalo kuti aiwale za iye chifukwa sadali kumufunanso. Izi zidaswa mtima wa Madalo poganizira momwe chikondi chawo chidalili ku sukulu yaukachenjede ija. Nkhaniyi idalephera kundipatsa nyonga zoti ndingamufunsire Madalo.

Tsiku lina tikukambirana za maphunziro athu, Madalo adandidabwitsa ndi momwe amandiyang'anira komanso makhalidwe ake. Kwa nthawi yoyamba, Madalo adakhala mondiyandikira kwambiri ndipo nthawi yonse tinkakambiranayo adali atagwira dzanja langa. Mopanda kufunsira kwenikweni chibwenzi chathu chidayamba mwamphamvu masiku owerengeka kuchokera pa tsikulo.

Patatha chaka chimodzi, Madalo adamaliza maphunziro ake ndipo adakayamba ntchito kutawuni yotchedwa Chitapa. Adapeza nyumba ku dera la Loziyayo. Patatha chaka chimodzi, inenso ndidatsiriza maphunziro anga ndipo ndidachita mphumi chifukwa nanenso ndidapeza ntchito kutawuni ya Chitapa komweko.

Titakwatirana, tidapeza nyumba yotakasuka ku dera la Maliwane. Uku ndi kumene moyo wathu udapita patsogolo kwambiri. Tidali anthu osangalala kwambiri ndipo tidatolera katundu osiyanasiyana chifukwa cha mgwirizano ndi chikondi chimene chidali pakati pathu. Tidapezanso mwayi wogula nyumba yomwe tinkakhala ndi galimoto zopuma ziwiri. Tinkachita zonsezi ine osadziwa kanthu.

Pano mpamene ndikudziwa kuti ubwenzi wa Madalo ndi Mayeso udakhala ukupitirirabe ngakhale adali pabanja. Ankatumizirana zithunzi, ndalama komanso

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

5. **(Mafunso akupitirira)**

mauthenga achikondi palamya. Mayeso adakanika kukhazikika ku Ulaya kuja ndipo adabwerera kumudzi kuno mwachinunu. Ngakhale lero Madalo akuti katundu yense nditenge ndipo sindidzamvanso za iye, ndikukhulupirira kuti akudziwa kuti wathawitsa gawo lina la mtima wanga ndipo moyo wanga sudzakhalanso chimodzimodzi. Mtima wamnzako ndi tsidya linadi.

**Mafunso**

a. (i) Kodi Madalo adamangitsa ukwati ndi ndani?

______________________________

**(Malikisi 1)**

(ii) Tchulani komwe sukulu ya ukachenjede yomwe Madalo ankaphunzirako idali.

______________________________

**(Malikisi 1)**

(iii) N'chifukwa ninji Madalo adapezeka akulira m'nyumba yowerengera mabuku kusukulu ya ukachenjede kuja?

______________________________

______________________________

**(Malikisi 2)**

(iv) Perekani zinthu **ziwiri** zomwe Madalo ndi mwamuna yemwe adakwatirana naye ankafanana ali kusukulu.

______________________________

______________________________

**(Malikisi 2)**

(v) Tsimikizani popereka mfundo imodzi kuti Madalo ndi amene adayambitsa kuti pakhale ubwenzi pakati pa iye ndi mwamuna yemwe adakwatirana naye.

______________________________

______________________________

**(Malikisi 2)**

Mafunso akupitirita/...

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

5. a. **(Mafunso akupitirira)**

(vi) Tchulani dera lomwe Madalo adapeza nyumba atayamba ntchito kutawuni ya Chitapa.

____________________________________________ **(Malikisi 1)**

(vii) Ndi zinthu **ziwiri** ziti zimene Madalo adanamiza mwamuna amene adakwatirana naye?

____________________________________________

____________________________________________ **(Malikisi 2)**

(viii) Tsimikizani kuchokera mu nkhaniyi kuti mtima wamnzako ndi tsidya linadi.

____________________________________________

____________________________________________ **(Malikisi 2)**

(ix) Perekani zinthu **ziwiri** zomwe Madalo ndi Mayeso ankatumizirana.

____________________________________________

____________________________________________ **(Malikisi 2)**

b. Kusanthula chiyankhulo

(i) Pezani mawu mu nkhaniyi omwe akufanana matanthauzo ndi awa:

1. chiphe ____________________ **(Malikisi 1)**

2. mphongo ____________________ **(Malikisi 1)**

(ii) Kuchokera mu nkhaniyi, pezani nsinjiro zachiyankhulo zomwe matanthauzo ake ndi awa:

1. chidayambitsa zonsezi ____________________ **(Malikisi 1)**

2. olemera ____________________ **(Malikisi 1)**

3. adawawidwa ____________________ **(Malikisi 1)**



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**Gawo C** (Malikisi 15)

**Chifupikitso**

6. **Werengani nkhani yotsatirayi mosamala. Nkhaniyi ili ndi mawu 153 ndipo muifupikitse kuti ikhale ndi mawu osachepera 50 komanso osapitirira 55.**

## KUFUNIKA KWA NTCHITO ZA MALONDA M'DZIKO

Malonda ndi mchitidwe wogula ndi kugulitsa katundu osiyanasiyana. Pali mitundu ikuluikulu iwiri ya malonda. Mitunduyi ndi malonda a pachiweniweni ndi malonda a pakati pa mayiko.

Kawirikawiri malonda a pachiweniweni amathandiza anthu kupeza zinthu zoyendetsera moyo wawo watsiku ndi tsiku monga zakudya, mankhwala komanso mayendedwe. Malonda a pakati pa mayiko nthawi zambiri amathandiza dziko lino kukhala ndi mwayi wotumiza kutundu wake makamaka wochokera ku ntchito zaulimi ku misika ya kunja kwa dziko lino. Uku kutha kukhala ku mayiko a mu Afirika momwe muno kapena mayiko aku Ulaya monga Britain, France ndi Germany. Dziko lathu limapeza kuchokera ku mayikowo zinthu monga zipangizo zopangira zinthu m'mafakitale kuphatikizapo makina ogwiritsa ntchito m'mafakitalemo. Malonda a pakati pa mayikowa amatithandizanso kupeza ndalama ya kunja ya dola ya America imene ndi yofunika kwambiri pa dziko lonse la pansi.

Tiyeni ngati dziko tilimbikire kuchita malonda a mitundu yosiyanasiyana kuti tithe kutukula moyo wathu watsiku ndi tsiku komanso chuma cha dziko lino.

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

6. **(Mafunso akupitirira)**

______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________
______________________________________________________________

**(Malikisi 15)**

**Gawo D** (Malikisi 15)

**Chimasuliro**

7. **Masulirani nkhani yotsatirayi m'Chichewa chomveka bwino.**

**CONFLICT RESOLUTION**

There are a number of strategies that may be used to resolve conflicts peacefully. Each strategy depends on the nature of the conflict. One such strategy is negotiation. Negotiation is a process whereby people involved in a conflict talk to each other about their problem. Through this, the people try to reach a solution that is acceptable to all. Negotiation is a positive way of resolving conflicts.

Peaceful conflict resolution helps to maintain long lasting peace between parties involved in a conflict.

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

7. (Mafunso akupitirira)

(Malikisi 15)

**MAFUNSO ATHERA PANO**

**NB: Pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi atatu.**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com